



Ena mwa amene adachita maphunzirowo

Apempha mafumu kuvomereza anthu kulembetsa malo

WOLEMBA:
MARTIN GELA

Mafumu m'dziko lino awapempha kuti avomereze anthu awo kulembetsa malo awo m'ndondomeko ya malo a makolo kuti akhale ndi zitupa za umwini wa malowa.

Mfumu yaikulu Mwansambo ya m'boma la Nkhotakota idanena izi masiku apitawa ku Bangula m'boma la Nsanje pomwe a amachitira umboni ntchito yophunzitsa makomiti oyendetsa ntchitoyi m'dera la T/A Mbenje m'bomalo.

A Mwansambo adati: "Ntchitoyi ndi yofunikira popeza ikuteteza anthu osauka kuphatikizapo amayi kuti akhale ndi zitupa za malo zomwe zidzathandizire kuti ngakhale ana awo akhale wotetedzwa kwa anthu ofuna kuti awalande malowa. Ndiipo adzakhala akuwagwiritsabe ntchito moyo wonse."

Iwo adati si zobisa kuti takhala tikuluza malo kwa makampani osiyanasiyana amene amabwera m'madera mwathu pongowagulitsa



CHITHUNZI: MARTIN GELA

A Mwansambo: Tisataye malo kwa obwera

motaya. Ndiipo adaonjeza kuti m'madera ena, makamaka m'phepete mwa nyanja, malo adagulitsidwa mtengo wotsika kwa azungu, zimene sizipindulira eni nthaka.

Malinga ndi mfumuyo, makomitiwa akuyenera kugwira ntchito mwa dongosolo potengera kuti mukomiti iliyonse muli

gulupu ndi amayi atatu ndi abambonso atatu.

Mkulu woyendetsa ntchitoyi m'maboma a Nsanje ndi Chikwawa a Colby Kabango adati akuwaphunzitsa makomitiwa momwe angagwirire ntchitoyi potsatira malamulo a dziko lino omwe anakonzedwa ndi Nyumba ya Malamulo. A Kabango anati khumbo

la boma n'kuteteza anthu kuti akhale ndi umwini wa malo pokhala ndi zitupa zomwe n'zofunikira kwa wina aliynse makamaka amayi.

Modzi mwa akuluakulu a kukhonsolo ya boma la Nsanje a Ellen Bikoko anati makomitiwa athandizira kuthetsa milandu ya malo yomwe yakula kwambiri m'bomalo.

A Zainabu Hussein wochokera ku komiti ya Tambo Customary Land Committee anati maphunzirowa awathandizira kuti anthu akhale ndi umwini wa malo pokhala ndi zitupa.

Iwo adati: "Tionetsetsa kuti pogawa malire, anthu onse okhudzidwa akupezeka komanso kukupewa kulandira ziphuphu zomwe makomiti onse 14 tagwirizana."

Ntchito yolembedsa malo a makolo akuigwira m'maboma a Nsanje ndi Chikwawa ndi thandizo lochokera ku bungwe la Shire Valley Transformation Programme (SVTP) ndi ndalama zochokera ku Global Environmental Facility (GEF). ■

**BWALO LA
ULIMI**



WOLEMBA: ANDREW SAUKANI

Kutaya nthawi nzopanda pake

Nthawi zino alimi ali otangwanika kugulitsa zokolola. Ambiri amaona ngati iyi ndi nthawi ya tchuthi pa ulimi motero anthu amangoledzera, kumangoyenda m'zisangalalo zosiyanasiyana ena kumakonzana maulendo kwa achibale.

Izi n'zabwino chifukwa imafunika nthawi ina kumapepuzako thupi osamgokhalira kugwira ntchito koma izi zisachite kutidyerana nthawi yonse mpaka kudziwala popeza ulimi wa masiku ano, oganiza bwino ndi amene zimamupindulira.

Ino ndi nthawi imene mlimi atha kupanikiza ulimi wa ndiwo za masamba uku akudikira kuyamba kusosa munda kukonzekera ulimi wa chaka chino. Mongokumbutsana alimi tikufunika kukhala tcheru ndi zochita zathu mosadzinamiza kuti nthawi ikanalipo poguliratu zipangizo za ulimi makamaka fetereza.

Zipangizo za ulimi zikuoneka kuti sizidzakhazikika monga kale koteru kugona pakati n'kuyambirira.

Lero tiunikirane zina mwa zimene zimatitaita nthawi ndipo tikuyenera kuzipewa.

Kusakonzekera zochita zatsiku lina zimampangitsa munthu kukhala opanda zochita motero wina akangoti tiyeni ku mowa ulendo umakhala omwezo.

Kubwereza zolakwika zomwezo nthawi ndi nthawi zimasonyeza kuti munthu sakufuna kuphunzira ndi kusintha koteru alimi pamene sitinachite bwino, tivomereze ndi kukonzana ndipo tisadzabwerezenso kulephera kotereko.

Alimi tiyeni tidziwe kuyamika pamene ena akuchita bwino maka anzathu alimi otsogola. Tisadzifanizire ndi ena amene akuchita bwino kapena zikuwayendera koma tiphunzire kwa iwo chifukwa kusatero kawirikawiri zimabala mkwiyo kapena nsanje.

Tionetsetsa kuti zimene tikuchita zisakhale zosangalatsa munthu pozindikira kuti sitingakwanitse kusangalatsa aliynse. Tichite zimene tikuona kuti zingathandize kutukula maanja anthu. Tiyeni tisamalekeze panjira ntchito imene taziya kale, tionetsetsa kuti taimaliza kufikira ku mapeto kuti tione pamene tachita bwino ndi magawo ofuna kukonza.

Alimi chonde tisangokhalira kudandaula osachitapo zinthu pothana ndi mavuto amene tikudutsamo. Ndi bwino kuwambenthulira anzathu za zipsinjo zimene tikukumana nazo chifukwa amati vuto mukalipereka kwa ena kumakhala kuti theka lakonzedwa.

Kumangodandaula nthawi zonse palibe chimene chingayende komanso izi zitha kukhala chimodzi mwa zifukwa zimene anthu ambiri akumangoganiza zodzipha basi.

Tiyenera kukhala olimba mtima osangochita mantha ndi zina zili zonse. Tiziyeserako kumachita zina zimene zingatithandize kusintha pa miyoyo yathu. Alimi nthawi zina zinthu zikumativuta kaamba kosafuna kugawa ntchito kwa anthu ena.

Kumapezeka kuti mlimi akungokakamira khasu yekha pa munda tsiku lonse chonsecho, ndalama zilipo zimene akanatha kulembera aganyu kuti amuthandize.

Tiphunzira kugawana ndi ena.

Pomaliza, alimi tisiye mamveramvera kuti anthu aziti chiyani ndikapanga ichi.

Inde ngati zimene mukufuna kuchita sizabwino, chonde siyani koma ngati ndi zabwino yeselani mosalabadira zolankhula za anthu ena. Zaitthwa! ■

Mafunso: saukaniandrew@gmail.com